# Kusamalila Manyowa ndi kupanga manyowa a madzi

## Malangizo a alimi ang'ono

### Kugwilitsila nchito manyowa a zinyama posamalila nthaka yabwino

- Manyowa a zinyama atanthauza ndowe za ziweto zazikulu ndi zazing'ono.
- Manyowa a zinyama ndi gawo yofunika kwambili ya ulimi wophataniza nyama ndi mbewu umene colinga cake n'kucepetsa kapena kulekelatu kugwilitsila nchito feteleza wamankhwala.
- Manyowa a ziweto ndi gwelo yochipa ya zakudya zopatsa thanzi pakukula kwa mbewu ndipo amathandiza kwambili kusunga conde m'nthaka kwanthawi yaitali.

### Kodi kusamalila manyowa n'kucita ciyani?

- Kusamalila manyowa kumatanthauza ndondomeko yotsatila ndi zocita zolowetsedwamo kuti mutenge, musunge, musamalile ndi kugwilitsila nchito manyowa.
- Pamafunika cisamalilo coyenela kuti munthu apeze zabwino kwambili kucokela ku manyowa a ziweto.
- Kusamalila bwino manyowa kumathandizanso kucepetsa kuipitsidwa kwa cilengedwe ndi zovuta zina monga fungo, nchenche tulombo toyambitsa matenda, ndi ina zotelo.
- Kusamalila bwino manyowa kungathandize kupewa matenda a ziweto monga zithupsa, zilonda m'kamwa, chipsela, ndi matenda ena omwe amacititsidwa ndi matope ndi manyowa onyowa/osauma. Manyowa ouma amapanga nguwi imene imacititsa mavuto a kupuma ku ng'ombe.

Zinthu zimene zimakhudza zakudya zipezeka m'manyowa ndi kukhalapo kwake kuti mbewu ikule bwino kumaphatikizapo: (i) Njila yosonkhanitsila ndi kosungila; (ii) Njila ndi nthawi yothila m'munda; (iii) kaya manyowa athilidwa mwacindunji kapena akonzedwanso kukhala feteleza/manyowa wa zowolela/oganiki monga kompositi kapena Bokashi.

### Kodi manyowa a madzi n'ciyani?

- Manyowa a madzi/Feteleza wamadzi umakonzedwa mwa kuviika m'madzi zowolela/kompositi, Bokashi, manyowa a ziweto kapena masamba okhala ndi zakudya/michele zambili kwamasiku angapo.

Zotsatilazi ndi zina mwazabwino zocheza manyowa a madzi:

- N'zosavuta kukonza - mosiyana ndi njila yopanga zowolela/feteleza zolimba, njila yopangila manyowa a madzi n'yosavuta komanso yopepuka.
- Mbewu imagwilitsila nchito msanga mukathila manyowa a madzi - cifukwa zakudya/michele zinasungunuka kale m'madzi, mbewu imayamba kudya nthawi yomweyo.
- Palibe zida zodula zimene zimafunikila kukonzela n'kugwilitsila nchito madziwa.

***Condo dziwani:** ngakhale pali mapindu ambili, manyowa a madzi sangalowe m'malo mwa feteleza wolimba wa zowolela/oganiki koma kuonjezela/kuthandizila.*

Promotion of agroforestry supported by:
unique land use
COMACO
Prepared by: Daniel M. Kalala
With support from
Federal Ministry of Food and Agriculture
by decision of the German Bundestag

## Njila zabwino zosamalila manyowa




**Kucepetsa dzuwa ndi mvula yofikapo pa manyowa mmene mungathele:** Kuika manyowa padzuwa kumapangitsa Nitrogen kuwonongeka monga ammonia yosungunuka; kusiya pa mvula zakudya/michele zonse zimasukika ndi madzi. Manyowa ayenela nthawi zonse azikhala pamthunzi kapena kuphimbidwa monga mungathele.




**Khola yoyenelela ya ziweto kuti asungike bwino ndi kusonkhanitsa manyowa:** Khola yabwino ya ziweto imathandiza kusonkhanitsa manyowa ndi kusungika bwino. Khola ya ziweto yopanda tsindwi/mtenje monga momwe zimakhalila ambili kumapangitsa kukhala kovuta kwambili kutola ndi kusunga manyowa.




**Wonjezelani mphamvu za manyowa a zinyamba/ziweto mwa kupanga feteleza wa zowolela:** Feteleza wa zowolela monga kompositi kapena Bokashi uli n'mapindu ambili monga kuculuka ndi mitundu-mitundu ya twamoyo tosaoneka n'maso (micro-organims); mulibe njele za udzu; zowola zagaika kale conco zakudya n'zosavuta kutengedwa ndi mbewu; palibe ciopsezo cotentha mbewu; ndi zina.




**Kugwilitsila nchito monga pogona m'khola** - Kachitidwe kameneka kamaonetsetsa kuti ndowe zonse za ziweto pamodzi ndi mkodzo zagwela paudzu. Kucotsa nthawi zonse zoyala/manyowa m'khola n'kuika pamthunzi zimatsimikiza kuti zakudyazo zasungidwa ndi kuwoletsa (kuwola pamalopo) ndikololedwa kuyamba.




**Kuthila/kuika feteleza wa manyowa/zowolela/oganiki moyenelela:** Kuthila pamalo amodzi kumalimbikitsidwa kusiyana ndi kuwaza. Feteleza wapansi, gwilitsilani nchito manyowa a oganiki mumaenje obzala kapena mum'folo. Ngati n'feteleza wapamwamba thilani munsi mwa mbewu musanayambe kupalila kuti muphimbe polima. Kumwaza kumawononga, kusiya manyowa padzuwa ndi pamvula komanso paudzu amatha mwamsanga.




**Mlingo wothila manyowa/feteleza wa oganiki m'munda:** Mosiyana ndi feteleza wa mankhwala umene mlingo n'woikika, palibe mlingo uliwonse pothila manyowa cifukwa kuculuka kudalila pa zifukwa zambili. Mwacitsanzo, tumathini tuwili twa coca-cola pobzala ndi mathini awili pa milungu itatu kapena inayi mbewu zikamela mungathile. Mathini awili a coca-cola n'cimodzi-modzi ndi kudzadza manja awili.

## Ndondomeko yotsatila popanga manyowa a madzi (feteleza wa madzi)




Ikani pafupifupi 30kg ya manyowa, kompositi, Bokashi kapena zomela za zakudya/michele yambili n'zowolela(biomass) mu thumba ya 50kg. Kusakaniza zinthu zambili kumapeleka zotsatila zabwino. Mangani thumba ku kamtengo n'kulowetsa mu dilamu ya 210 L ya madzi. Phimbani dilamu ndi thumba kapena ciliconse kuti musalowe nchenche, koma kulola pempho iziyenda.




Gunduzani thhumba/saka kawili pa tsiku, m'mawa ndi madzulo kwa milungu iwili kapena itatu. Kugwedeza saka kumacitika mwa kucotsa cophimba pamwamba n'kugunduza kamtengo kumene mwamangilila thumba kwa mphindi zitatu kapeana zisanu. Pambuyo pa milungu iwili kapena itatu, manyowa akonzeka mungagwilitsile nchito.




Thilani kugwilitsila nchito sipuleya kucotsako komwazila kapena thilani ndi bekete/thini kutapila n'kapu. Nthaka ikhale yonyowa pothila manyowa a madzi. Mlingo wothila umasiyana kuyambila 100ml mpaka 300ml malinga ndi mtundu wa mbewu, siteji ya kukula ndi conde ca nthaka mmene cilili.